wa Aloma?
-Ayi.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anapita ku Yelusaremu?

-Yesu anapita kukaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.



## PHUNZIRO LA 64

1.Kodi nanga ngati munthu ali ndi chuma pa dziko la pansi pano, chumacho chikamuthandiza iye akadzapita ku chilango chosatha?
-Ayi.

2.Kodi chuma chingatipulumutse ife ku tchimo imfa ndi Satana?
-Ayi.

3. Kodi chinachitika ndi chiyani kwa mulimi wachuma uja?
-Mulungu anamuyitanira iye ku imfa.

4. Kodi amene anasankha tsiku limene anamwalira mulimi wachuma uja anali ndani?
-Mulungu yekha.

5. Ngakhale kuti mulimi wachuma uja anali ndi chuma chambiri, kodi ankasoŵa chiyani?
-Moyo osatha.

6. Kodi chofunika kwambiri kuposa chuma chambiri ndi chiyani?
-Kukhulupilira mwa Mulungu ndikukhala ndi moyo osatha.

7. Kodi tikudziŵa bwanji kuti nkhani imeneyi ndi yeniyeni?
-Chifukwa chakuti anthu aŵiri ameneŵa anakhalako pa dziko la pansi pano.

8. Kodi munthu akafa, mzimu wache umapita kuti?
-Kwa Mulungu, kumwamba, kapena ku gahena, ku malo a moto ndi chilango chosatha.

9.Kodi pali malo ena oyembekezera pakati pa dziko la pan-si ndi kumwamba?

-Ayi.

10. Kodi munthu wachuma uja, choyamba anamupempha Aburahamu kuti achite chiyani?
-Anamupempha Aburahamu kuti amutume Lazaro kuti aviike msonga ya chala chake m'madzi kuti akaziziritse lilime lache.

11. Kodi anthu onse amene amakhulupilira mwa Mulungu adzapita kuti akadzafa?
-Kukakhala ndi Mulungu kumwamba.

12. Kodi anthu onse amene akukana kukhulupilira mwa Mulungu, adzapita kuti akadzafa?
-Adzapita ku gahena ku malo a moto ndi chilango chosatha.

13. Kodi munthu amene adzalowe ku gahena adzathanso kuchokako?
-Ayi.

14. Kodi chachiŵiri chimene anapempha munthu wachuma uja kwa Aburahamu chinali chiyani?
-Munthu wachuma uja ankafuna kuti Lazaro akalankhule kwa abale ache kuti iwowo asadzavutike ngati m'mene ankavutikira iye ku malo amoto ndi chilango chosatha.

15. Kodi Aburahamu ankamuwuza munthu wachuma uja kuti abale akewo ayenera kuchita chiyani?
-Ankaŵawuza kuti iwo ayenera kuŵerenga ndi kumvera Buku la Mulungu, Bayibulo.

16. Ngati ife sitimvera Mawu a Mulungu ndikukhulupilira, pangakhalenso china chake chakuti chingatipulumutse ife?
-Palibe.



-Chomcho, ophunzira a Yesu aŵiri aja anapita m'mudzimo ndipo anakamupezadi buluyo ndikupita naye kwa Yesuyo.

-Kodi ophunzira a Yesu aja atabwera naye buluyo , chinachitika ndi chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 11:7-10

7-Ndipo iwo anbwera naye mwan wa buklu uja kwa Yesu, nayika zovara zawo pa iye, ndipo Iye anakhala pamenepo.
8-Ndipo anthu ambiri anayala zovala zawo pa njira, pamene ena ankayala zitsamba zimene ankazidula ku minda.
9-Ndipo iwo amene anatsogolera pamodzi ndi otsatira omwe anafuwula kuti, “Hasana!” “Alemekezedwe Iye wakudza mu dzina la Ambuye!”
10-“Ulemekezeke Ufumu umene uli mkudza, wa atate athu, Davide!” “Hosana wa kumwambamwamba!

-Yesu anakhala pa buluyo ndipo anakwera mpaka mu mzinda wa Yelusalemu.

-Ngati m'mene Mulungu ananenera kwa aneneri ache, Yesu analowa mu Yelusalemu pa bulu.

-Pamene Yesu ankalowa mu Yelusalemu anthu ankafuwula mosangalala.

-Kodi chifukwa chiyani anthu ankasangalala ndi Yesu ndikumalankhula za ufumu wa davide umene unali kudza?

-Chifukwa chakuti anthu ankaganiza kuti Yesu akupita kukaŵapulumutsa iwo ku ulamuliro wa Aloma.

-Kodi Yesu ankapita kukaŵapulumutsa iwo ku ulamuliro

emu, Yesu anaŵalamulira ena mwa ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 11:1-6

1-Ndipo pamene iwo anayandikira ku Yerusalemu, ku Betefage ndi Betaniya, pa phiri la Azitona, anatuma aŵiri mwa ophunzira ache,

2-nati, “Pitani, loŵani m’mudzi umene uli patsogolo panuwo, ndipo mukangoloŵa, mukapeza mwana wa bulu omangidwa, amene sanakweredweko ndi munthu wina aliyense. Mukam’masule ndipo mukabwere naye.

3-Ndipo munthu wina aliyense akakakufunsani kuti , “Kodi chifukwa chiyani mukuchita zimenezi?” mukamuwuze kuti, “Ambuye akumufuna ndipo adzamutumiza kuno posachedwapa.”

4-Ndipo iwo anapita, nakamupeza mwana wa bulu ali omangidwa pa khomo, pa bwalo, m’khwalala, namumasula iye,

5-anthu ena amene anayima pamenepo, anafunsa kuti, “Kodi mukuchita chiyani, mukumasula mwana wa buluyo?”

6-Iwo anayankha ngati m’mene Yesu anaŵawuzira, ndipo anthuwo anaŵasiya kuti adzipita.

-Kodi chimeneYesu anaŵalamulira aŵiri mwa ophunzira ache, chinali chiyani?
-Anaŵalamulira kuti apite m’mudzi umene unali patsogolo pawo ndipo akamasule mwana wa bulu ndikumupititsa kwa Iye.

-Kodi Yesu ankaba buluyo?
-Ayi.

-Yesu anaŵawuza ophunzira achewo kuti akaŵawuze eni buluyo kuti akabwera nayenso.



-Kodi Yesu anati kuti anabwera pa dziko la pansi pano chifukwa chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:45

45-[Yesu anati] “Pakuti ngakhale Mwana wa munthu sanabwere pa dziko la pansi kudzatumirikidwa, koma kutumikira ndi kupereka moyo wache kukhala dipo (chiwombolo) kwa anthu ambiri.”

-Kodi Yesu anabwera pa dziko la pansi ndi cholinga chakuti ife tidzimutumikira Iye kapena kuti tidzitsata njira yathuyathu yopitira kumwamba?
-Ayi.

-Yesu satipempha ife kuti timupatse Iye china chilichonse.

-Yesu satipempha ife kuti timuchitire Iye china chake.

-Yesu ndi Mulungu, chomcho Iye safuna china chilichonse.

-Yesu ali ndi china chilichonse chimene Iye amafuna.

-Yesu sanabwere pa dziko la pansi kuti anthu adzimutumikira Iye.

-Yesu anati kuti Iye anabwera pa dziko la pansi pano kudzaŵatumikira anthu.

-Yesu analankhulanso kuti Iye anadza pa dziko la pansi kudzapereka moyo wache ngati dipo (chiwombolo) la anthu ambiri.

-Pamene Yesu ndi ophunzira ache ankachoka mu mzinda wa Yeriko, anakumana ndi munthu wa khungu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:46

46-Ndipo iwo anafika ku Yeriko; ndipo pamene Iye anali kuturuka mu Yeriko ndi ophunzira ache, pamodzi ndi khamu lalikuru la anthu, mwana wa Timeyu, Batimeyu, wopempha wa khungu, anali kukhala pansi m'mbali mwa njira.

-Kodi dzila la munthu wopempha, wakhunguyo, anali ndani?
-Batimeyu.

-Kodi khungu la Batumeyu, likutikumbutsa ife chiyani za anthu onse?
-Anthu onse anabadwa ndi khungu ngati Batumeyu.

-Kodi anthu onse anabadwa bwanji ndi khungu?
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, iwowo anasanduka kukhala a khungu kwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, anasanduka kukhala a khungu ku zowona zenizeni za Mulungu.

-Chifukwa chakuti anthu onse anabadwa mwa Adamu ndi Hava, anthu onse amabadwa ali a khungu kwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti anthu onse anabadwa mwa Adamu ndi Hava, anthu onse ndi akhungu ku zowona zenizeni za Mulungu.

-Ngati m'mene sankathera kuwonera Batumeyu, ifenso sitikutha kuwona zowona zenizeni za Mulungu.

-Kodi Batumeyu anakatha kupanga china chilichonse kuti



-Kodi Batumeyu ankafuna kuti Yesu amuchitire chiyani iye?

-Batumeyu ankafuna kuti Yesu amubwezere kuwona kwache.

-Kodi Yesu anakatha kumubwezera Batumeyu kuwona kwache?
-Inde.

-Kodi Batumeyu ankakhulupilira kuti Yesu amubwezera kuwona kwache?
-Inde.

-Kodi Yesu anamubwezera Batumeyu kuwona kwache?
-Inde.

-Yesu analankhula kuti chifukwa cha chikhulupiliro cha Batumeyu, kuwona kwache kubwelera kwa iye.

-Nthaŵi yomweyo Yesu anamubwezera Batumeyu kuwona kwache.

-Kodi ndi ndani yekha amene anatha kupereka kuwona kwa Batumeyu?
-Yesu.

-Ndi Yesu yekha amene anatha kupereka kuwona kwa munthu wa khungu.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga maso onse, ndi Mulungu yekhanso amene angathe kupereka kuwona ku maso athu.

-Yesu ndi ophunzira ache atayandikira mzinda wa Yelusal-

-Kodi Mulungu amaŵasamalira anthu onse?
-Inde.

-Munthu aliyense ndi ofunika kwa Mulungu.

-Ngakhale tifupike ola titalike, ife tonse ndi ofunika kwa Mulungu.

-Ngakhale tide ola tiyere, ife tonse ndi ofunika kwa Mulungu.

-Ngakhale tilemere ola tisawuke, ife tonse ndi ofunika kwa Mulungu.

-Ngakhale tidwale ola tisadwale, ife tonse ndi ofunika kwa Mulungu.

-Ngakhale tikhale a nzeru ola opanda nzeru, ife tonse ndi ofunika kwa Mulungu.

-Kodi Mulungu sakonda munthu wina aliyense ndikufuna kumupulumutsa?
-Ayi.

-Kodi Batumeyu anachita chiyani Yesu atamuyitana iye?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:50-52

50-Ndipo iye anataya chofunda chake, nadzuka, nadza kwa Yesu.
51-Ndipo Yesu anamufunsa kuti, “Kodi ukufuna kuti ndikuchitire chiyani?” Ndipo wa khunguyo anati kwa Iye, “Mphunzitsi, ndilandire kuwona kwanga.”
52-Ndipo Yesu anati kwa Iye, “Pita, chikhulupiliro chako chakupulumutsa. Iwe.” Ndipo nthaŵi yomweyo anapenya, namutsata Iye pa njira.



achotse khungu lache?
-Ayi.

-Kodi anthu akhoza kutha kupanga china chakwe kuti achotse khungu lawo kuti athe kuwona zowona zenizeni za Mulungu?
-Ayi.

-Ngati m’mene anakalephelera kuchotsa khungu lache Batumeyu, chomchonso anthu onse alibe chimene angachite kwa iwo okha kuti achotse khungu lawo kuti awone zowona zenizeni za Mulungu.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kupelera kuwona kwa Batumeyu?
-Yesu.

-Kodi ndi ndani yekha amene angathe kupereka kuwona kwa anthu onse?
-Yesu.

-Ngati m’mene anathera Yesu yekha kupereka kuwona kwa Batumeyu, chomchonso ndi Yesu yekha amene angathe kupereka kuwona ku maganizo a anthu onse kuti athe kumvetsetsa zowona zenizeni za Mulungu.

-Kodi Batumeyu anamutcha Yesu kuti ndani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:47

47-Ndipo atamva kuti ndi Yesu wa ku Nazarete, anayamba kufuwula, nati, “Yesu, Inu Mwana wa Davide mundichitire ine chifundo!”

-Kodi Batumeyu anamutcha Yesu kuti ndani?
-Mwana wa Davide.

-Kodi chifukwa chiyani Batumeyu anamutcha Yesu Mwana wa Davide?
-Chifukwa chakuti Yesu anali chidzukulu cha Mfumu Davide chimene Mulungu analonjeza kuti chidzakhala Mpulumutsi.

-Batumeyu anadziŵa kuti sangathe kudzithandiza yekha.
-Batumeyu anadziŵa kuti munthu amene angathe kumuthandiza iye ndi Yesu yekha.

-Chifukwa chakuti Batumeyu anali atamva za zozizwitsa zambiri zimene ankachita Yesu, anamuyitana Yesu kuti amuthandize iye.

-Batumeyu anamupempha Yesu kuti amumvere chisoni iye.

-Batumeyu ankadziŵa kuti sanali oyenera kuchizidwa chifukwa cha tchimo lache.
-Batumeyu anadziŵa kuti sanakatha kulipira kuchizidwa kwache.

-Batumeyu anadziŵa kuti ngati Yesu akumuchiza iye, ikhala mphatso yawulele yochokera kwa Mulungu.

-Ife tonse tili ngati Batumeyu.

-Chifukwa chakuti tachimwa, sitili oyenera kuti tichizidwe.

-Chifukwa chakuti mphoto ya tchimo ndi imfa, sitili oyenera kuti tilipire china chilichonse kuti tichizidwe..

-Ngati tingachizidwe, ndiye kuti ndi mphatso yawulele yochokera kwa Mulungu.



-Kodi anthu anati chiyani atamumva Batumeyu akumuyitana Yesu?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:48

48-Ndipo anthu ambiri anamudzudzula kuti atontholе, koma iye anapitirizabe kufuwula kwambiri kuti, “Mwana wa Davide, mundichitire ine chifundo!”

-Kodi chifukwa chiyani anthu anamuletsa Batumeyu kumuyitana Yesu pomuwuza kuti akhale chete?
-Anthu ankaganiza kuti Yesu sankafuna kuchiza munthu wa khungu ndipo opempha wa umphaŵi.

-Kodi zimenezo zinali zowona?
-Ayi.

-Kodi Yesu sankafuna kuti amuthandize munthu wa khungu ndipo opempha wa umphaŵi?
-Ayi.

-Yesu akufuna kuthandiza munthu wina aliyense.

-Ngakhale kuti anthu anamuletsa iye ndikumuwuza kuti akhale chete, Batumeyu anapitirizabe kulilira kwa Yesu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 10:49

49-Ndipo Yesu anayima, nati, “Muyitaneni. Ndipo anamuyitana wa khunguyo, nanena naye kuti, “Limba mtima, nyamuka akukuyitana.”

-Ngakhale kuti Batumeyu anali wa umphaŵi wa khungu, kodi Yesu anamusamalabe iye?
-Inde.